# DIOCESE OF CHIKWAWA

## KULENGEZA ZA KUKHAZIKITSIDWA KWA PARISHI YATSOPANO

*Saint Joseph, Chinthebe*

❖ ❖ ❖

Poganizira ntchito yopatulika ya Mpingo yofikira mitundu yonse ya dziko lapansi, komanso motsogoleredwa ndi kufunika kwa chibalalitso cha Mpingo kukhala wa anthu onse (Catholic) ndi kumvera lamulo la Yesu Khristu, Muyambitsi wake (Marko 16:16), lolengeza Mthenga Wabwino kwa anthu onse; ndipo

Poganizira kuti atumwi eni ake, omwe Mpingo unamangidwa pa iwo, potsatira mapazi a Khristu, "analalikira uthenga wa wa choona ndi kukhazikitsa mipingo" (LG, 23); ndi udindo wa olowa m'malo mwao kupititsa patsogolo ntchitoyi "kuti Mau a Mulungu afalikire ndi kulemekezedwa" (2 Atesalonika 3:1) ndipo Ufumu wa Mulungu ulengezedwe ndi kukhazikitsidwa padziko lonse lapansi;

Poganizira kuti ndi ufulu wa Bishopu wa Dayosizi kukhazikitsa ma parishi atafunsa Bungwe la Ansembe ndi Bungwe la Akhristu eni ake mu dayosizi; ndipo

Choncho, nditakwaniritsa kutsatira zofunikira zonse ndi potsatiranso malamulo a Mpingo, ndipo mogwirizana ndi ulamuliro womwe waperekedwa ku udindo wanga mu lamulo la Mpingo. (Cf. Canon 515, §2;),

Ine, **Bishopu Peter Musikuwa wa Dayosizi ya Chikwawa**, kudzera mu chikalatachi, ndikukhazikitsa **Saint Joseph, Chinthebe**, imene pakali pano ili pansi pa parishi ya Njale, ngati Parishi ya dera (territorial parish) mu Dayosizi ya Chikwawa. Parishi yatsopanoyi idzakhala gawo la Deanery ya Molere. Choncho, kuyambira tsopano idzatchedwa Saint Joseph, Chinthebe Parishi.

Parishi yatsopanoyi idzakhala ndi matchalitchi ang'onoang'ono (out-stations) awa: **Mankhamba, Chisinkha, Jeremiah, Masamba, Mbendera, Mapanga ndi Wilson**. Matchalitchiwa adzakhalanso ngati malire a dera la parishiyi:

Ndikulengeza kuti chigamulochi chifalitsidwe pa webusaiti ya Dayosisi ya Chikwawa, yomwe idzatengedwa ngati njira yovomerezeka yodziwitsira anthu za nkhaniyi. Komanso, chigamulochi chiyenera kuikidwa pamalo owoneka bwino kuti anthu onse a mu parishiyo adziwe za nkhaniyi. Uthengawu udziwitsidwe kwa akhristu onse. Onse amene adzasonkhana mu parishi yatsopanoyi ayeretsedwe polandira ma Sakramenti kawirikawiri, ndipo akule ndi kuzama m'chikhulupiriro ndi utumiki; komanso ubale wawo ndi Yesu Khristu pamodzi ndi amnzao.

Pomaliza, ndikulengeza kuti **Bambo Yohane Nzondola** asankhidwa kukhala **Bambo Mfumu woyamba** wa Parishi ya **Saint Joseph, Chinthebe**, ndipo adzakhala ndi ulamuliro ndi udindo woperekedwa ndi Malamulo a Mpingo (Canon Law).

Kukhazikitsidwa kwa Parishi ya Saint Joseph mu Dayosisi ya Chikwawa kudzayamba kugwira ntchito pa tsiku Loweruka, **pa 29 mwezi wa Ogasiti**, chaka cha 2026, tsiku lokumbukira masautso a Yohane Mbatizii Woyera.

Uthengawu waperekedwa lero pa tsiku la **1 mwezi wa Ogasiti, chaka cha 2026**, tsiku lokumbukira Saint Alphonsus Liguori, Bishopu ndi mphunzitsi wa Mpingo.

**Right Reverend Peter Musikuwa**
*Bishop of the Diocese of Chikwawa*

**Very Reverend Father Cosmas Chasukwa**
*Vicar General*